15. Iwo adzawala monga dzuŵa. Iwo adzakhala mu Ufumu wa Atate. Koma nthaŵi ya chimaliziro siinafike. Ana a Mulungu ali kukhala pakati pa ana a woipayo. Zimenezi zimaoneka ngati kuti sizikusintha. Ana a woipayo amaseka chifukwa iwo amapitirizabe kukhala m'machimo.

Kuchokera m'nthano ya namsongole, kodi chidzaoneka ndi chiyani kwa namsongole kapena ana a woipayo pa chimaliziro cha nthaŵi?

---

================================================================

16. Iwo adzaponyedwa pa moto.

Mateyu 13:42:
Kumeneko kudzakhala kulira ndi kukukuta mano.

Koma zimenezi sizidzachitika kwa olungama. Ana a Mulungu adzakhala ali kusangalala chifukwa chakuti akhala ali wokhulupirika kufikira nthaŵi ya chimaliziro.

Kodi ndi chiyani chimene chingadzaoneke kwa mbewu yabwino kapena ana a chilungamo a Mulungu pa chimaliziro cha nthaŵi?

---

================================================================

17. Iwo adzawala monga dzuŵa. Ifenso tidzawala monga dzuŵa ngati tiri wokhulupirika. Ife tiyenera kuganiza za zimenezi pamene tikukhala m'moyo wovuta wa Chikhristu. Tiyenera kuganizira za zimenezi pamene anthu oipa ali kutiseka ife. Tiyenera kuganizira za zimene pamene ali kutiyesa kuti tichite zoipa. Ife kuwala monga dzuŵaku sitidziŵa kutanthauza kwake. Koma tikudziŵa kuti ife tidzakhala ndi Mulungu. Ife tidzaunika monga Iye ali kuunika. Sitidzayesedwa kuti tichimwenso.

Mwina inu mukudziŵa Mkhristu amene ali ndi mavuto. Pitani kamuuzeni zomwe mwaphunzira mphunziro ili. Muonetseni mphotho yomwe ili kumuyembekezera iye ngati ali wokhulupirika. Mukhale okonzekera kuuza kalasi zomwe iye wanena.

================================================================

18. Kuchokera mu nthano ya namsongole, kodi ndi chiyani chomwe chidzaoneke kwa namsongole kapena ana a woipayo pa nthaŵi ya chimaliziro cha nthaŵi?

______________________________

Kodi ndi chiyani chidzaoneke kwa mbewu yabwino kapena kwa ana a chilungamo a Mulungu?

______________________________

______________________________

SABATA LACHISANU NDI CHINAYI: KHRISTU APHUNZITSA ANTHU AMBIRI
TSIKU LACHITATU: UFUMU WA MULUNGU UFANANA NDI CHUMA

1. Kaŵirikaŵiri Yesu anali kuphunzitsa anthu ndi nthano. Nthanoyo inali kuthandiza anthu kuti amvetsetse. Nthano inali kuŵathandiza kuti azindikire chomwe anali kuphunzitsa.

Kuchokera m'nthano ya namsongole, kodi ndi chiyani chimene chidzaoneke kwa namsongole kapena ana a woipayo pa nthaŵi ya chimaliziro cha nthaŵi?

____________________________________________________________

Kodi ndi chiyani chidzaoneke kwa mbewu yabwino kapena ana olungama a Mulungu?

________________________________________________________

==========================================================================

2. Pa chimaliziro cha nthaŵi ya pansi pano, ana a Satana adzaponyedwa kumoto. Koma ana a Mulungu adzawala monga dzuŵa. Zimenezi ndi zimene Yesu anaphunzitsa m'nthano ya namsongole.

Posachedwa Yesu ananena nthano ya Ufumu wa Mulungu. Iye anafotokoza za chuma cha m'munda. Chuma ndi kanthu kena kabwino. Ndi chinthu cha mtengo wapatali. Anthu ambiri amafuna kukhala nacho, motero mwini wake ayenera kuchisamala bwino. Zimenezi ndi zimene Yesu anaphunzitsa.

> Mwa nthano ya chuma chobisika ndi ngale ya mtengo wake, Yesu anaphunzitsa kuti ife tiyenera kulola kusiya zonse ndi kutsata Yesu.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Mateyu 13:44 kulekeza 46. Werenganinso ndime 44. Kodi ndi chiyani chofanana ndi chuma chobisika m'munda?

________________________________________________________

==========================================================================

3. Ufumu wa Kumwamba uli monga chuma. Dzulo tinaphunzira mmene ana a Ufumu angadzapatsidwire mphotho. Iwo adzawala monga dzuŵa. Iwo adzakhala mu Ufumu wa Atate wawo. Pano pa dziko lapansi adzakhala ali kusautsidwa ndi zoipa zambiri. Iwo ayenera kukhala pafupi ndi ana a woipayo

Koma ndi chinthu chabwino ndi chodabwitsa kukhala mwana wa Ufumuwo. Ndi chinthu chabwino koposa china chilichonse chimene tingakhale nacho pa dziko lapansi.

Kodi ndi ndani amene anaphunzitsa nthano ya chuma chobisika kuonetsa kuti ife tiyenera kukhala wololela kusiya zonse chifukwa cha Khristu?

______________________________________________________________________

==========================================================================

4. Khristu mwina anaphunzitsa zimenezi. Anali Yesu. Iye ananena nthano ziŵiri za nkhaniyi kuti athandize anthu kuti amvetsetse. Taonaninso pa nthano ya chuma cha munda.

Mateyu 13:44:

> Ufumu wa kumwamba uli wofanana ndi chuma chobisika m'munda; chimene munthu anachipeza, nachibisa; ndipo m'kuchikonda kwake anachoka, nagulitsa zonse ali nazo nagula munda umenewu.

Kodi munthu anachita chiyani kuti apeze ndalama zogulira munda umene munali chumacho?

______________________________________________________________________

==========================================================================

5. Munthu anagulitsa zonse zimene anali nazo. Iye anadziŵa kuti ndi chuma chodabwitsa. Ngati akadachipeza, kukanakhala kwabwino koposa zinthu zina zonse anali nazo. Yesu anati njira imeneyi ndi imene tiyenera kuchitira ndi Ufumu wa Kumwamba.

Kodi ife tiyenera kulola kusiya chiyani kuti titsate Khristu?

______________________________________________________________________

==========================================================================

6. Tiyenera kulola chilichonse. Zimenezi zitikumbutsa ife za mawu a Yesu amene taphunzira kale.

Luka 14:26:

> Munthu akadza kwa Ine, wosada atate wake ndi amake,

ndi mkazi wake, ndi ana ndi abale, ndi alongo ake, inde ndi moyo wake womwe wa iye mwini, sakhoza kukhala wophunzira wanga.

Kodi ndi ufumu wa yani umene tiyenera kukhala wofunitsitsa kusiira zilizonse?

---

---

==========================================================================

7. Tiyenera kukhala olola kusiya zonse chifukwa cha ufumu wa Khristu kapena Mulungu. M'nthano imene Yesu anainena, anthuwo anagulitsa zonse zimene anali nazo. Iwo anazigulitsa chifukwa chofuna kugula zinthu zimene anazipeza. Zimenezi ndi zimene Yesu anazinena. Iye anagulitsa zonse zimene anali nazo kuti agulenso anthu ake. Zimenezi zimationetsa zimene ife tiyenera kuchita. Tiyenera kukhala wolola kusiya zilizonse pofuna kutsata Khristu.

Kodi ndi nthano yoyamba iti imene Yesu anaifotokoza pophunzitsa zimenezi?

---

==========================================================================

8. Ndi nthano ya chuma chobisika m'munda. Ndipo Yesu ananena nthano ina yophunzitsa phunziro lomweli.

Mateyu 13:45:

> Ndiponso Ufumu wa Kumwamba uli wofanana ndi munthu wa malonda wakufuna ngale zabwino; ndipo mmene anaipeza ngale imodzi ya mtengo wapatali anapita nagulitsa zonse anali nazo, naigula imeneyo.

Ngale ndi mwala wa mtengo wapatali omwe umakhala ndi anthu olemera. Akazi olemera nthaŵi zina amavala ngale m'makosi awo. Ngale ndi zokongola kwambiri. Ndi za mtengo wapamwamba kwambiri. Anthu ena amakhala ndi miyala yoyera yomwe imaoneka ngati ngale, koma sizikhala ngale zenizeni. Ngale zenizeni zimakhala za mtengo wapamwamba.

M'nthano iyi ya Yesu, kodi ndi chiyani chifanana ndi ngale?

---

==========================================================================

9. Ufumu wa Mulungu uli monga ngale. Munthu anali kuyang'ana kanthu kena kabwino. Iye anapeza ngale yabwino kwambiri. Iye anadziŵa kuti inali yoyenera kukhala nayo kuposa zinthu zonse. Iye anadziŵa kuti kutsogolo idzamuthandiza.

Anthu ena amaika chuma chawo pa ng'ombe zawo. Ena amaika chuma chawo ku Banki. Ena amapereka chuma chawo kwa abwenzi kuti aŵasungire Ena amakumba maenje ndi kuchikwirira.

Munthu wa m'nthano yachiŵiriyi anadziŵa kuti ngale inali chinthu chabwino. Iye anadziŵa kuti ngaleyo inali yabwino yosungira ndalama zake.

Kodi munthu anachita chiyani kuti apeze ngale? ____________________

______________________________________________________________

==============================================================

10. Munthu anagulitsa zonse zimene anali nazo. Iye anagula ngale. Iye anakondwera. Anadziŵa kuti wachita chinthu chabwino. Iye anadziŵa kuti ngaleyo inali chinthu choposa katundu wina aliyense.

Kodi ife tiyenera kulolela kuchita chiyani kuti titsate Khristu?

______________________________________________________________

==============================================================

11. Tiyenera kukhala wololela kusiya zonse zimene tili nazo. Zimenezi siziri kutanthauza kuti tipite tikagulitse akatundu athu onse amene tili nawo. Chimatanthauza kuti pamene tikusankha, tizisankha Khristu. Ngati tingapande kupitiriza kutsata miyambo ina ndi kutsata Khristu, tikhoza kusiya miyambo imeneyi. Ngati sitingapitirize kugwiritsa ntchito ya mtundu wina ndi kutumikia Khristu, tikhoza kusiya ntchitoyo. Khristu anasiya ulemerero wake m'mwamba kuti adzalipire machimo athu.

Afilipi 2:5-8:

> Khristu Yesu...sanachiyesa cholanda kukhala wofana ndi Mulungu...anadzikhuthula yekha, natenga maonekedwe a kapolo, nakhala m'mafanizidwe a anthu; ndipo popezedwa m'maonekedwe ngati munthu, anadzichepetsa yekha, nakhala womvera kufikira imfa, ndiyo imfa ya pamtanda.

Ife tiyenera kulolela kusiya zonse tiri nazo m'malo mofuna kuchita chiyani?

______________________________________________________________

12. Ife tiyenera kukhala wololela kuchita zimenezi m:malo motsata Khristu. Munthu amene anali ndi chuma anaona kuti chinali chabwino koposa zonse anali nazo. Wogulitsayo anaona kuti ngale inali yabwino koposa zimene anali nazo. Yesu anaona kuti kutipulumutsa ife kunali kwabwino koposa zonse zimene anali nazo m'mwamba. Ifeyo ndife chuma chake choposa kwa Iye.

Kodi ndi phunziro lotani limene Yesu anaphunzitsa pa nthano ya chuma chobisika ndi ngale ya mtengo wake?

______________________________

______________________________________________________

==========================================================

13. Phunziro limene iye anaphunzitsa ndi ili: Ife tiyenera kukhala wololela kusiya zonse zimene tili nazo pofuna kutsata Khristu. Yesu Khristu ndi chuma chachikulu. Iye anatichitira zambiri ife. Anatipulumutsa kuchokera ku imfa. Anatipatsa ife moyo watsopano. Anatipatsa nyumba zathu kapena abwenzi athu pomutsata Iye. Tiyenera kulolela kusiya malo athu a ulemu ndi kumutsata Iye.

Kodi Yesu ananena nthano ziŵiri ziti pofuna kutiphunzitsa ife zimenezi?

(1) ______________________________________________

(2) ______________________________________________

==========================================================

14. Nthano zake zinali: Chuma chobisika ndi ngale ya mtengo wapatali. Anthu onsewo anagulitsa zonse zimene anali nazo. Yesu anachoka kumwamba ndi kudza kwa ife. Iye anasiya kwawo ku Nazarete napita kukalalikira ndi kukachiritsa. Iye anapereka moyo wake pa mtanda chifukwa cha ife. Iye anachita zimenezi chifukwa anadziŵa kuti ife ndife a mtengo wapatali.

Kodi ndi phunziro lotani limene Yesu anaphunzitsa pa nthano ya chuma chobisika ndi ngale ya mtengo wapatali?

______________________________

______________________________________________________

==========================================================

15. Nthano ndi yakuti: Ife tiyenera kukhala wololela kusiya zonse pofuna kutsata Khristu. Anthu ayenera kusiya kwawo. Iwo ayenera kusiya abwenzi awo kapena ntchito zawo. Mtumwi Paulo anati anasiya zinthu zonse:

Afilipi 3:8:

> Komatu zenizeninso ndiyesa zonse zikhale chitayiko chifukwa mapambanidwe a chizindikiritso cha Khristu Yesu Ambuye wanga; chifukwa cha Iyeyu ndinatayikitsa zinthu zonse, ndipo ndiziyesa zapadzala, kuti ndikadzionjezere Khristu.

Kodi inu munasiyako kanthu kena m'malo mofuna kutsata Khristu?

______________________________

Ngati munatero, lembani kanthu kena kamene munakasiyako.

____________________________________________________________________

========================================================================

16. Tidzakambirana za zimenezi tonse limodzi.

Kodi ndi phunziro lotani limene Yesu anaphunzitsa ndi nthano ya chuma chobisika ndi ngale ya mtengo wapatali?

______________________________

____________________________________________________________________

____________________________________________________________________

========= ==============================================================

SABATA LACHISANU NDI CHINAYI: KHRISTU APHUNZITSA ANTHU AMBIRI
TSIKU LACHINAYI: IYE ANAONETSA MPHAMVU YAKE PA ZINTHU ZONSE

1. Yesu anaphunzitsa kwambiri kupyolera mu nthano.

Kodi ndi phunziro lotani limene Iye anaphunzitsa mwa nthano ya chuma chobisika ndi ngale ya mtengo wapatali?

______________________________

________________________________________________________________

==========================================================================

2. Iye anaphunzitsa kuti ife tiyenera kukhala olola kusiya zonse pofuna kutsata Khristu. Nthaŵi zina zimenezi zimakhala zovuta kwambiri. Koma potsatira Khristu pali zinthu zabwinonso. Yesu anatikonda ife. Iye amatithandiza m'miyoyo yathu. Yesu anachita zozizwitsa zinayi zimene anaonetsa kuti ali ndi mphamvu ya pa anthu onse. Iye anatontholetsa mphepo pa nyanja. Iye anatulutsa ziŵanda kwa munthu wotchedwa Legiyo. Iye anachiritsa mkazi wa nthenda yokha mwazi. Iye anaukitsa mwana wa mkazi wa Yairo atamwalira. Kuchokera ku zozizwitsa zimenezi tikuphunzira kuti Yesu anali ndi mphamvu kuposa zinthu zinayi.

(1) Chilengedwe
(2) Ziŵanda
(3) Matenda
(4) Imfa

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Luka 8:41 mpaka 55. Kodi Yesu anali ndi mphamvu yothandiza Yairo?

______________________________

==========================================================================

3. Yesu anathandiza Yairo. Iye ali ndi mphamvu yoposa imfa. Iye ali ndi mphamvu yoposa zinthu zina. Yesu anaphunzitsa ophunzira ake ndi mawu amene ananena. Anaŵaphunzitsa ndi ntchito imene Iye anachita. nawaonetsa kuti anali ndi mphamvu yoposa chilengedwe. Chilengedwe chimatanthauza mphepo ndi mvula ndi dzuŵa, komanso dziko limene Mulungu analilenga.

Luka 8:22-23:

> Ndipo panali limodzi la masiku aja, Iye analoŵa m'ngalawa, ndi ophunzira ake; nati kwa iwo, "Tiolokere ku tsidya lija la nyanja." Ndipo anakankhiramo. Ndipo mmene iwo anali kupita pamadzi, Iye anagona tulo. Ndipo panyanja panatsikira

namondwe wa mphepo; ndipo podzala ndi madzi, anali kuopsedwa.

Kodi munthu wamba ali ndi mphamvu m'mawu ake pa chilengedwe?

---

==========================================================================

4. Munthu aliyense alibe mphamvu yoposa chilengedwe. Iye alibe mphamvu yoposa mphepo ndi mvula. Koma Yesu ali ndi mphamvu imeneyi. Iye anaonetsa akuphunzira ake mphamvu yake.

Luka 8:24:

> Ndipo anadza kwa Iye, namuutsa, nanena, Ambuye, Ambuye, titayika. Ndipo anauka, nadzudzula mphepo ndi mafunde ake a madzi; pomwepo zinaleka, ndipo panagwa bata.

Kodi Yesu anaonetsa motani mphamvu yake kuposa chilengedwe?

---

==========================================================================

5. Yesu anatontholetsa mphepo. Iye anaidzudzula ndipo mphepo inaleka. Yesu anali munthu. Iye anali ndi thupi longa lathu. Anali kumva njala ndi kufuna chakudya. Iye anali kutopa ndi kufuna kupumula chogona. Koma Yesu anali woposa munthu. Mawu ake ndi ntchito yake imaonetsa zimenezi. Taonani zimene Iye ananena.

Yohane 5:17-18:

> "Atate wanga amagwira ntchito kufikira tsopano, Inenso ndigwira ntchito." Chifukwa cha ichi Ayuda anaonjezera kufuna kumupha...Chifukwa amatchanso Mulungu Atate wake wa Iye yekha; nadziyesera wolingana ndi Mulungu.

Pamene Yesu anatontholetsa mphepo, kodi zimenezi zinaonetsa mphamvu yake yoposa chiyani?

---

==========================================================================

6. Zimenezi zinaonetsa mphamvu yake yoposa chilengedwe. Mphepo inasiya ndipo nyanja inakhala bata. Ngalawa inatheka kuoloka nyanja. Pambali ina Yesu anapeza munthu wotchedwa Legiyo. Legiyo amatanthauza kuti ambiri. Munthu amene anali kutchedwa Legiyo chifukwa ziŵanda zambiri kapena mizimu yoipa inali mwa iye. Yesu analamulira mizimu kuti ituluke mwa iye.

Taphunzira za zimenezi. Kodi ife timadziŵa bwanji kuti Yesu ali ndi mphamvu yoposa ziŵanda?

________________________________________

____________________________________________________________

=========================================================================

7. Ife timadziŵa zimenezi chifukwa iye anatulutsa ziŵanda mwa anthu. Iye anatulutsanso ziŵanda mwa munthu ameneyunso. Ziŵanda zinapempha kuti zilowe m'gulu la nkhumba. Zinaloledwa kuchita chomwecho. Zimenezi zimaonetsa kuti munthu mmodzi ndi wofunika koposa nyama zambiri.

Luka 8:25:

> Ndipo iwo anatuluka kukaona chimene chinachitika; ndipo anadza kwa Yesu, nampeza munthuyo, amene ziŵanda zinatuluka mwa iye, alikukhala pansi ku mapazi ake a Yesu wovala ndi wanzeru zake; ndipo iwo anaopa.

Kodi ndi ndani anaonetsa mphamvu yake kuti ndi yoposa ziŵanda pomasula munthu wotchedwa Legiyo?

________________________________________

=========================================================================

8. Yesu anachita zimenezi. Anthu anadabwa ndipo anachita mantha. Koma munthu wotchedwa Legiyo anali wokondwa. Iye anamasulidwa. Iye anafuna kupita ndi Yesu, koma Yesu anamuuza kuti:

Luka 8:39:

> "Pita kunyumba kwako, nufotokozere zazikuluzo anakuchitira iwe Mulungu."

Pamene Yesu anamasula munthu uyu, kodi mphamvu yake inaposa chiyani?

__________________________________________________

=========================================================================

9. Inaonetsedwa mphamvu yake yoposa ziŵanda. Yesu anali ndi mphamvu yoposa matenda. Ife taona zozizwitsa zambiri za machiritso. Mphunziro lalero munthu wotchedwa Yairo anabwera kwa Yesu. Iye anapempha Yesu kuti apite kunyumba kwake ndi kukachiritsa mwana wa mkazi wake. Koma pa njira kanthu kena kanachedwetsa.

Luka 8:43-44:

> Ndipo mkazi, anali ndi nthenda yachidwarire zaka khumi ndi ziŵiri, amene adasudzula asing'anga za moyo wake zonse, ndipo sanathe kuchiritsidwa ndi mmodzi yense, anadza pambuyo pake, nakhudza mphonje ya chovala chake, ndipo pomwepo nthenda yake inaleka.

Lembani zinthu ziŵiri zoyamba zimene Yesu anali ndi mphamvu yoziposa.

(1) ____________________ (3) Matenda

(2) ____________________ (4) Imfa

==========================================================================

10. Zozizwitsazo zinaonetsa kuti Yesu anali ndi mphamvu yoposa chilengedwe ndi yoposa ziŵanda. Koma tsopano mkazi anabwera kwa Yesu. Iye sanapemphe Yesu kuti amukhululukire. Kapena mwina panali anthu ambiri ali kulankhula ndi Yesu. Mwina iye anali ndi mantha wofunsa. Koma mkaziyo anakhulupirira kuti iye akhoza kumuchiza. Ndi chikhulupiriro iye anakhudza mphonje ya chovala chake. Nthaŵi yomweyo anachiritsidwa. Iye anakhala ali kudwala kwa zaka khumi ndi ziŵiri. Tsopano anali bwino.

Pamene Yesu anamuchiritsa iye, kodi iye anaonetsa mphamvu kuposa chiyani?

______________________________________________________________________

==========================================================================

11. Chimenechi chinaonetsa mphamvu yoposa matenda. Mphepo inabwera mwadzidzidzi pa akuphunzira. Koma mkazi ameneyu anavutika kwa zaka khumi ndi ziŵiri. Yesu anaŵathandiza onsewo. Inu muyenera kukumbukira zimenezi mukamakhala ndi mavuto. Zilibe kanthu ngati mavuto anu abwera modzidzimutsa kaya mwakhala nawo kwa zaka zambiri. Uzani Yesu za mavutowo. Iye akhoza kukuthandizani.

1 Petro 5:7:
Ndi kutaya pa Iye nkhaŵa yanu yonse, pakuti Iye asamalira inu.

Kodi Yesu ali ndi mphamvu zoposa chilengedwe, ziŵanda, matenda ndi imfa?

________________________________________

======================================================================

12. Iye ali ndi mphamvu yoposa zonsezo. Yesu anadziŵa kuti mkazi wachiritsidwa. Iye anati, "wandikhudza ndani?"

Luka 8:47-48:
Ndipo mkaziyo pakuona kuti sanabisika, anadza ndi kunthunthumira, nagwa pamaso pake, nafotokoza pamaso pa anthu onsewo chifukwa chake cha kumkhudza Iye, ndi kuti anachiritsidwa pamenepo. Ndipo Iye anati kwa iyeyo, "mwana wanga, chikhulupiriro chako chakupulumutsa iwe; muka ndi mtendere."

Zozizwitsa za Yesu zinaonetsa mphamvu yake kuposa zinthu zotani?

(1) ____________________ (3) ____________________

(2) ____________________ (4) Imfa

======================================================================

13. Zozizwitsa zake zinaonetsa mphamvu yake yoposa pa chilengedwe, ziwanda, matenda ndi imfa. Chinatenga nthaŵi kuti alankhule ndi mkazi wochiritsidwayo. Yesu anafuna kuti adziŵe kuti chinali chikhulupiriro chimene chinalola kuti iye achiritsidwe.

Luka 8:49:
Mmene Iye anali chilankhulire, anadza wina wochokera kwa mkulu wa sunagoge, nanena, "mwana wako wafa; usavutitse Mphunzitsi."

Kodi munthu ameneyu anaganiza kuti Yesu ali ndi mphamvu yoposa imfa?

________________________________________

======================================================================

14. Iye anaganiza kuti Yesu sakanakhoza kuchita kanthu kalikonse tsopano. Yairo anali mkulu wa m'sunagoge yemwe Ayuda anali kukapembedzako. Koma iye analibe mphamvu yoposa imfa. Iye anakonda mwana wake. Koma sakanakhoza kumuthandiza mwanayo. Tsopano wamwalira.

Luka 2:50,54:

> Koma Yesu anamva, nayankha, kuti, "Usaope; khulupira kokha; ndipo iye adzapulumutsidwa." ...anagwira dzanja lake naitana nati, "Buthu, tauka."

Kodi ndi chozizwa chotani chimene chinaonetsa mphamvu ya Yesu yoposa imfa?

________________________________________

========================================================================

15. Poukitsa mwana wa mkazi wa Yairo kunaonetsa mphamvu ya Yesu yaikulu. Yairo anaganiza kuti Yesu akanakhoza kuchiritsa msungwanayo. Iye sanadziŵe kuti Yesu akadakhoza kumuukitsa kwa akufa. Iye anadabwa. Iye anaona kuti Yesu sanali munthu chabe. Yesu anauza Yairo kuti asauze anthu zomwe zaoneka. Yesu sanafune kuti anthu amutsatire Iye chifukwa cha zozizwitsa.

Pamene Yesu anautsa mwana wa mkazi wa Yairo, kodi chimenechi chinaonetsa kuti anali ndi mphamvu ya chiyani?

__________________________

========================================================================

16. Zimenezi zinaonetsa mphamvu kuposa imfa. Zozizwa zina zinaonetsa mphamvu yoposa pa zinthu zina. Iye anatontholetsa namondwe pa nyanja. Iye anamasula munthu wotchedwa Legiyo. Iye anachiritsa mkazi wa nthenda ya msambo.

Kodi ndi pa zinthu zotani zozizwitsa zinaonetsa mphamvu ya Yesu?

(1) ____________________ (3) ____________________

(2) ____________________ (4) ____________________

========================================================================

17. Zozizwitsa zimenezi zinaonetsa mphamvu ya Yesu yoposa chilengedwe, mizimu ndi matenda. Mphamvu yotere ikadapanga anthu ena kukhala onyada.

Iye amatikonda ndipo amafuna kutithandiza.

Kodi kuukitsidwa kwa mwana wa mkazi wa Yairo kunaonetsa kuti Yesu ali ndi mphamvu pachiyani? ____________________

=====================================================================

18. Kuukitsidwa kwa mwana wa mkazi wa Yairo kunaonetsa mphamvu yake yoposa imfa. Taona kuti Yesu akhoza kuchita chilichonse kuchokera mphunziro limeneli. Iye ali ndi mphamvu yoposa zinthu zonse zimene zimativuta ife.

Kodi pamene munda wanu ukhala ndi mvula yambiri kapena pang'ono muyenera kuchita chiyani? ____________________

____________________

Lembani chinthu chimodzi chimene Yesu anakuchitirani kuonetsa mphamvu yake. ____________________

=====================================================================

19. Tidzakambirana za zimene tonse pamodzi.

Zozizwitsa zinayi izi zinalembedwa pa Luka 8: Kutontholetsa mphepo, kumasula munthu wotchedwa Legiyo, kuchiritsa mkazi wa nthenda ya msambo, ndi kuukitsa mwana wa mkazi wa Yairo. Kodi zozizwitsa zimenezi zili kuonetsa mphamvu ya Yesu yoposa zinthu zinayi zotani?

(1) ____________________ (3) ____________________

(2) ____________________ (4) ____________________

=====================================================================

SABATA LACHISANU NDI CHINAYI: KHRISTU APHUNZITSA ANTHU AMBIRI
TSIKU LACHISANU: KHRISTU ATUMA OPHUNZIRA KUTI AKALALIKIRE NDI KUCHIRITSA

1. Sabata ino taona mmene Yesu anaphunzitsira anthu. Iye anaphunzitsa mwa kunena komanso zimene anali kuchita.

– Zozizwitsa zinayizi zinalembedwa pa Luka 8: Kutontholetsa namondwe, kumasula munthu wotchedwa Legiyo, kuchiza mkazi wa nthenda, ndi kuukitsa mwana wa mkazi wa Yairo. Kodi zozizwitsazi zimaonetsa mphamvu ya Yesu yoposa zinthu zinayi zotani?

(1) ____________________ (3) ____________________

(2) ____________________ (4) ____________________

==================================================================

2. Zimaonetsa mphamvu ya Yesu yoposa pa chilengedwe, ziŵanda, matenda ndi imfa. Yesu anali kuphunzitsa anthu ndi zimene Iye anali kuchita. Iye yekha anaphunzitsa anthu. Iye anafunanso kuti akuphunzira ake aziŵaphunzitsa. Iye anali kukonza ophunzira kuti akonzekere kupita kwina. Mphunziro lathu la lero tiona mmene Iye anaŵatumizira aŵiriaŵiri. Yesu anaŵatumiza kwina:

(1) Kukalalikira Ufumu.
(2) Kukachiritsa anthu.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Luka 9:1 mpaka 9. Kodi ndi akuphunzira angati amene Yesu anaŵatumiza pa nthaŵi imeneyo?

______________________________________________

==================================================================

3. Iye anatumiza khumi ndi aŵiri. Ameneŵa anali ophunzira ake apadera. Ife taona mmene Iye anaŵasankhira iwo. Taona mmene Iye anaŵaphunzitsira iwo. Iwo anali naye pamene anali kuchiritsa anthu ndi kukalalikira Ufumu wa Mulungu. Iwo anali kuona Yesu ali kuchita zinthu zimenezi. Tsopano iwo ayenera kuzichita okha.

Kodi iwo anali kukalalikira Ufumu chifukwa chakufuna kwawo kapena kuti iwo anatumidwa?

_ ______________________________________________________________

==========================================================================

4. Iwo anapita chifukwa chakuti anatumidwa. Iwo anatumidwa kukachita zinthu ziŵiri. Iwo anayenera kulalikira ndi kuchiritsa. Iwo anayenera kuuza anthu ndi kuŵathandiza. Ifenso lero tinatumidwa kunja. Tinatumidwa kuti tikathandize anthu.

Luka 9:2:

Ndipo anaŵatuma kukalalikira Ufumu wa Mulungu, ndi kukachiritsa anthu odwala.

Kuchokera m'ndime imeneyi, kodi Yesu anaŵatuma kuti akalalikire za chiyani?

__________________________________________________________________

==========================================================================

5. Iwo ayenera kulalikira za Ufumu wa Mulungu. Pa nthaŵi imeneyi akuphunzira anapita kwa Ayuda kukalalikira. Ayuda anali atadziŵa kale za Mulungu. Koma iwo anayenera kulapa. Iwo anayenera kukhulupirira pa Yesu. Mdani wa Mulungu sanafune kuti Ayuda akhulupirire mwa Yesu. Iye anagwira ntchito motsutsana ndi Yesu. Iye anayeneranso kugwira ntchito motsutsana ndi akuphunzira.

Luka 9:1:

Ndipo Iye anaitana pamodzi khumi ndi aŵiriwo nawapatsa mphamvu ndi ulamuliro pa ziŵanda zonse, ndi zakuchiritsa nthenda.

Ziŵanda ndi atumiki a Satana. Kodi Yesu anapatsa ophunzira chiyani choposera pa ziŵanda kuti akhoze kulalikira bwino za ufumu?

_______ _____ _____________________________________________

==========================================================================

6. Yesu anapatsa mphamvu ophunzira kuti apose ziŵanda. Satana ndi amithenga ake sakanatha kuŵaletsa iwo. Koma anthu ambiri anali ndi ziŵanda Mizimu yoipayi inali kubweretsa zovuta kwa anthu. Yesu anauza ophunzi-

ra kuti azitulutsire kunja kuchokera m'mitima ya anthu. Iwo anachita zimenezi m'dzina la Yesu. Ndipo anthu anali okonzekera kumva za Ufumu wa Mulungu.

Kodi akuphunzira anatumizidwa kukachita chiyani za Ufumu wa Mulungu?

____________________________________________________________

============================================================

7. Iwo anatumizidwa kukalalikira. Iwo analalikira za ufumu wa Mulungu. Chimenechi ndicho chinthu choyamba chomwe iwo anatumidwa kukachita.

Luka 9:2:

Ndipo anaŵatuma kukalalikira Ufumu wa Mulungu, ndi kukachiritsa anthu odwala.

Kodi ndi ndani ayenera kulalikira Ufumu wa Mulungu masiku ano?

____________________________________________________________

============================================================

8. Ife tiyenera kuchita zimenezi masiku ano. Akuphunzira khumi ndi aŵiri analalikira kwa Ayuda. Ayuda anaganiza kuti iwo amadziŵa zambiri za Mulungu. Iwo anali onyada chifukwa chakuti anali ana a Abrahamu. Iwo anaganiza kuti sanafunikire kulapa ndi kukhala ndi chikhulupiriro. Akuphunzira anayenera kuti aŵapange kuti amvetsetse.

Anthu ena masiku ano ali ndi maganizo omwewo pa za Mulungu. Ena amadziŵa zambiri za Iye. Koma ambiri sakhulupirira mwa Iye. Iwo samvera Iye. Sakhala chiwalo cha mu Ufumu wa Mulungu. Ife tiyenera kuŵapanga kuti amvetsetse.

Kodi chinthu choyamba chimene Yesu anatumizira ophunzira ake khumi ndi aŵiri kuti akachite chinali chiyani?

(1) ______________________________________________

(2) Kukachiritsa anthu

============================================================

9. Chinthu choyamba chinali kulalikira Ufumu wa Mulungu. Iwo anayenera kuonetsa anthu mmene angabadwire mwa tsopano ndi kuti akalowe mu Ufumu. Iwo anayenera kuthandiza anthu kuti akhulupirire mwa Khristu. Iwo ana-

yeneraso kuthandiza anthu ndi zovuta za m'miyoyo yawo.

Luka 9:1:

Ndipo Iye anaitana pamodzi khumi ndi aŵiriwo naŵapatsa mphamvu ndi ulamuliro pa ziŵanda zonse, ndi zakuchiritsa nthenda.

Kuchokera m'ndime imeneyi, kodi ndi mphamvu yotani imene Yesu anaipereka kwa ophunzira poonjezera mphamvu yoposa ziŵanda?

________________________

==========================================================================

10. Iye anaŵapatsa mphamvu yakuchiritsa. Taona kale kuti Yesu anali kusamalira anthu. Iye anasamalira za mabanja awo, ntchito yawo, ndi miyoyo yawo. Iye anafuna kuti athandize anthu. Motero Iye anaŵatumiza iwo kunja kuti akachiritse. Patapita nthaŵi pang'ono anthu odwala ambiri anabweretsedwanso kwa Yesu.

Luka 9:11:

Koma unyinji wa anthu, pamene anadziŵa, anamtsata Iye; ndipo Iye anawalandira. nalankhula nawo za Ufumu wa Mulungu, nachiritsa amene anasoŵa kuchiritsidwa.

Kuchokera m'ndimeyi, kodi Yesu anachita chiyani ndi anthu odwala?

____________________________________________________________________

==========================================================================

11. Iye anaŵachiritsa iwo. Iye anafuna kuti ophunzira zichiritsa anthu Pamene anthu anaona kuchiritsako, kunali kwapafupi kwa iwo kuti akhulupirire Yesu. Umo ndi mmene zinaonekera ndi Yohane Mbatizi. Iye anali ndi makaiko aza Yesu. Koma Yesu anauza anthu a Yohane kuti akamuuze iye mmene anthu anali kuchiritsidwira.

Luka 9:3-4:

Ndipo Iye anati kwa iwo, "musanyamule kanthu ka paulendo, kapena ndodo, kapena thumba, kapena mkate, kapena ndalama; ndipo musakhale nawo malaya aŵiri. Ndipo mnyumba iliyonse mukalowemo, khalani komweko, ndipo muzikachokera kumeneko.

Kodi akuphunzira anali kuyenera kupita nyumba ndi nyumba kumasonkhetsa ndalama chifukwa cha kuchiritsa kumene anachita? ___________________

==========================================================================

12. Akuphunzira sanali kuchiritsa anthu kuti azipeza ndalama. Iwo sanali kupita nyumba ndi nyumba kuti akadye chakudya chambiri. Iwo anali kupita kuti akathandize anthu.

Masiku ano timapeza anthu amene amayesa kuchiritsa anthu ndi mphamvu ya mizimu. Ndipo iwo amafuna ndalama zambiri chifukwa cha kuchiza kumene akuchita. Yesu anati, ophunzira ayenera kudyetsedwa, koma iwo sayenera kulipiritsa anthu chifukwa chowachiza. Kumbukirani ndi iyi.

Mateyu 6:33:

Koma muthange mwafuna Ufumu wako ndi chilungamo chake,
ndipo zonse zimenezo zidzaonjezedwa kwa inu.

Pamene ophunzira analalikira za Ufumu wa Mulungu ndi kuchiritsa, kodi iwo akadamapeza kuti chakudya ndi zovala zomwe iwo anazifuna?

__________________________________________________________________________

==========================================================================

13. Akuphunzira adzapatsidwa zinthu zimenezi. Anthu adayenera kukhala wothokoza chifukwa cha zimene ophunzira anachita. Iwo adayenera kukhala wokondwera kuti anachiritsidwa.

Bwanji ife? Pamene tikulalikira tiyenera kuthandiza anthu. Tiyenera kuŵapatsa kanthu kena kamene iwo angakhale wothokoza.

Kodi Yesu anatumiza ophunzira kuti akachite chiyani poonjezera kulalikira Ufumu wa Mulungu?

___________________________________________

==========================================================================

14. Iye anaŵatumiza kukachiza anthu. Monga munthu pa dziko lapansi; Yesu sakadatha kupita yekha kulikonse. Iye anatuma ophunzira kunja aŵiriaŵiri. Iye anayamba ndi akuphunzira khumi ndi aŵiri. Nthaŵi ina Iye anatumiza ophunzira ena ambiri. Iwo anayenera kukachita ntchito ya Yesu. Nthaŵi zonse anayenera kumutukula. Ndipo anthu akadakhoza kufuna kumutsa Iye.